Kodi Ndondomeko ya Zipangizo za Ulimi Zotsika Mtengo (FISPs) ndi chani?

Zipangizo zaulimi za mu dongosolo la Kukweza Ntchito za Malimidwe (Green Revolution) ndi mbeu zamakono, foteleza komanso mankhwala ophela tizilombo. Zipangizo zimenezi zimayenela kugulidwa – kawirikawiri kuchokela ku nthambi ya boma, anthu ogulitsa zipangizo zaulimi kapena makampani wopelekela zipangizo.

Liwu lakuti 'subsidy' limatanthauza kuti winawake apelekapo kenakake pothandiza alimi kugula zipangizo zimenezi. 'Winawakeyo' kawirikawiri ndi nthambi ya boma kapena kampani yopelekela zipangizo, ndipo 'kenakakeko' kawirikawiri ndi ngongole ya ndalama kapena dongosolo lina wa ngongole.

'Subsidy' limanveka ngati kuti boma kapena kampani zopelekela zipangizo zikuchita chinthu chabwino kwa alimi, KOMA alimi ayenela kukhala wosamala pa zotsatira zobwera pa nthawi yaitali pa ngongole zilizonse za ndalama kapenanso madongosolo ena angongole. Kawirikawiri izi zimatengela alimi ku msampha wa ngongole omwe mwinamwake sangathe kuwuthawa. Kodi chidzachitike ndi chani pamene mwakulephela kubweza ngongole?

african centre for biodiversity

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156

duducoelho.com